

Pemphero la Ambuye

Maphunziro a anyamata ndi atsikana a zaka 18-35

1. Atate wathu wa Kumwamba
 2. Dzina lanu liyeretsedwe
 3. Ufumu wanu udze
 4. Kufuna kwanu kucitidwe monga Kumwamba comweco pansu pano
 5. Mutipatse ife lero cakudya cathu calero
 6. Mutikhulukire ife mangawa athu, monga ifenso takhulukira amangawa anthu
 7. Musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo
-

Phunziro 1 Atate wathu wa Kumwamba

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Coko
- Bolodi

1. Kulandiridwa (10 min)

- Landirani onse pa kubwera kwao.
- Fotokozani kuti anyamata ndi atsikana adzaphunzitsidwa za Pemphero la Ambuye.
- M'phunziro lililonse tidzawerenga Baibulo cifukwa maphunziro onse akhala cabe pa zimene Baibulo likamba.

Zidziwitso:

- Maphunzirowa ndi a anyamata ndi atsikana a zaka 18-35.
- Phunziro lililonse lidzayamba pa nthawi ya koloko. Onse afike pa nthawi yake cifukwa ngati azicedwa sitidzakhala ndi nthawi yokwanira.
- Ndi cofunikira kwambiri kubwera ku maphunziro onse.
- Aphunzi ayenera kulowa ndi Baibulo m'maphunziro onse. Tidzalifuna pophunzira maphunziro a m'Baibulo.
- M'phunziro lotsiriza tidzalemba mayeso (aphunzitsi adzasankha ngati mayeso adzalembedwa). Kulemba mayeso sikudzakhala bvuto ngati mudzaphunzirako maphunziro onse!

Fotokozani malamulo

- Ana a zaka zocepera 18 sadzaloledwa, ndiponso osabwera ndi ana ang'ono-ang'ono.
- Osayenda-yenda (pitani ku cimbudzi musanayambe kuphunzira).
- Khalani bwino ndipo mverani bwino aphunzitsi anu. Khalani omasuka.
- Funsani ngati aphunzi ali ndi mafunso.
- Pemphani Mulungu dalitso la phunziro iri.

2. Mapemphero athu (15 min)

- Funsani aphunzi ngati amapemphera. Ngati inde, afunseni kumene amapemphera.
- Afunseni kuti amapemphera ciani. Lembani mayankho ao pa bolodi.
- Afunseni ndi cifukwa ciani amapemphera.
- Fotokozani zifukwa zake za kupemphera:
 1. Timadalira pa Mulungu. Iye ndiye Mlengi ndi Mwini wa miyoyo yathu. Tidalira pa Iye pa thanzi, mvula, nzeru ndi zina zonse. Timfunikanso m'miyoyo yathu ya uzimu: cipulumutso, ciyeretso ndi zinthu zina zonse.
 2. Kupemphera ndi njira yolemekesa Mulungu. Kupemphera ndi njira ya kubvomereza kuti Iye yekha ndiye Mulungu. Ayenera matamando athu ndi cipembedzo cathu. Kupemphera ndi njira yolemekesa pa zonse zimene atipatsa.
- Fotokozani kuti m'kupemphera kupatsidwa si kofunikira koposa koma ubwenzi. Nthawi zambiri kukonda kumakhalapo ngati pali kupatsidwa. Koma Mulungu afuna kuti timkonda nthawi zonse: ngati apatsa komanso ngati sapatsa.

3. Cifukwa cake ca kuphunzira Pemphero la Ambuye (10 min)

- Funsani aphunzi kuti adziwa bwanji kupemphera. Ndi yani amene anawaphunzitsa?
- Fotokozani kuti pamene Yesu anali pa dziko lapansi, ophunzira ake anamfunsa kuwaphunzitsa kupemphera ciani (Luka 11.1).
- Awerengereni Pemphero la Ambuye monga lalembedwa m'Mateyu 6.9-13.
- Fotokozani kuti tidzaphunzira za Pemphero la Ambuye cifukwa pempheroli ndi citsanzo ca pemphero limene tinalandira kwa Yesu yekha.
- M'Pemphero la Ambuye muli:
 1. Kulemekeza Mulungu
 2. Kupempha zosowa zathu za masiku onse
 3. Kupempha zosowa zathu za miyoyo yathu ya uzimu
 4. Kupempherera anthu ena
 Ndiye pemphero ilo ndi citsanzo ca mapemphero onse.

4. Kufotokoza za 'Atate wathu wa Kumwamba' (15 min)

- Auzeni aphunzi kuganizira za atate ao m'miyoyo yao: atate a m'thupi (mukamdziwa kapena musakamdziwa), amuna ena amene anatilera ndiponso amuna ena amene ali monga atate kwa ife.
- Fotokozani kuti m'miyoyo yathu ya masiku onse si onse ochedwa atate ndiwo atate abwino. Afunseni zimene atate abwino amacita. Tiyenera kupempherera atate oipa kuti asinthe makhalidwe ao oipa ndipo tiyenera kuwathandiza kuti alekadi zoipa.
- Pamene tinena 'Atate wathu' sitimapemphera atate athu a pa dziko lapansi koma Atate wina. Timapempha Mulungu. Mulungu ndi Atate wabwino.
- Pamene tinena 'Atate wathu' timaulula kuti:
 1. Mulungu ndi Mlengi wathu. Iye ndiye Atate wathu. Tifuna kulemekeza mwa kumucha 'Atate'.
 2. Ndife ana a Mulungu.
Ngati macimo athu akhululukidwa ndife ana a Mulungu: tiri m'ubwenzi ndi Mulungu (osafotokoza zambiri za mfundo iyi, cifukwa adzaiphunzira m'phunziro 6).
Fotokozani kuti ndi cotheka kunena kuti ndife ana a Mulungu koma si ndife ana ndithu. Kunena cabe kuti ndife ana a Mulungu sitipangitsa kukhala ana ake moonadi. Koma Yesu atembenuza anthu kukhala ana a Mulungu. Auzeni kuganizirako: 'Kodi ndine mwana wa Mulungu? Ndiloledwa kunena kuti Iye ndiye Atate *wanga?*'
- Tikamba '*wathu*' cifukwa Mulungu ali ndi ana ambiri omkhulupirira.
- Pamene tinena 'Kumwamba' tiulula kuti Mulungu ndi wamkulu wuposa anthu onse a pa dziko lapansi. Iye ndiye Wamphamvuyonse, Mwini, Wolamulira, Wodziwa zonse.

5. Kuwerenga Baibulo: Kodi Mulungu ndiye Atate wotani? (20 min)

- Aphunzi atsegule Baibulo lao.
- Werengani pamodzi [Luka 15.11-24](#).
- Pangani magulu ang'ono-ang'ono. M'gulu lililonse anyamata ndi atsikana ayenera kukambirana za mafunso awa (lembani mafunso pa bolodi):

Mafunso

1. Fotokozani zimene zinacitika m'nthano.
2. Mnyamata wamng'ono atazindikira kuti ku nyumba ya tate wake zonse zinali bwino, anabwereranso kwa tate wake. Nanga inu, munapita kale kwa Mulungu ndi kuulula macimo anu?
3. Kodi tate anacita ciani pamene anaona kuti mwana wake wamng'ono anabwerera? Kodi tate anakondwera?
4. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi zokhudza Mulungu Atate?

- Atakambirana m'magulu ang'ono, kambiranani pamodzi m'gulu lonse. Ngati mayankho sali bwino mukonze zolakwika. Mayankho abwino ali conco:

1. Fotokozani zimene zinacitika m'nthano.

Yankho: Tate anali ndi ana a amuna awiri. Mwana wa mwamuna wamng'ono anapempha gawo lake napita ku dziko lakutali kukakondwera kumeneko. Zitatha ndalama zake iye anazindikira kuti moyo udzakhala wobvuta. Anabwerera ku nyumba ya tate wake nabvomera kuti adacita zoipa. Pamene anafika kunyumba, tate wake anali kumyembekezera namcitira cifundo.

2. Mnyamata wamng'ono atazindikira kuti ku nyumba ya tate wake zonse zinali bwino, anabwereranso kwa tate wake. Nanga inu, munapita kale kwa Mulungu ndi kuulula macimo anu?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

3. Kodi tate anacita ciani pamene anaona kuti mwana wake wamng'ono anabwerera? Kodi tate anakondwera?

Yankho: Atate anathamanga, namkupertira pakhosi pace nampsonetsa. Anakondwera kwambiri.

4. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi zokhudza Mulungu Atate?

Yankho: Mulungu afuna anthu ocimwa kubwerera kwa Iye, Iye ndi wacifundo ndipo alandira ocimwa otayika onse amene abwerera kwa Iye.

6. Kuchula Pemphero la Ambuye (5 min)

- Kambani pamodzi Pemphero la Ambuye mpaka onse adziwa.

Atate wathu wa Kumwamba

Dzina lanu liyeretsedwe

Ufumu wanu udze

Kufuna kwanu kucitidwe monga Kumwamba comweco pansi pano

Mutipatse ife lero cakudya cathu calero

Ndipo mutikhulukire ife mangawa athu, monga ifenso takhulukira amangawa anthu

Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo

Cifukwa wanu uli ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero wa nthawi zonse

Amen

7. Kutsiriza (5 min)

- Bwerezaninso citanthauzo ca 'Atate wathu wa Kumwamba'.
- Tsirizani ndi pemphero.

Phunziro 2 – Dzina lanu liyeretsedwe

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Coko
- Bolodi

1. Kulandiridwa (5 min)

- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezaninso mwachidule zimene zinakambidwa m’phunziro 1 .

2. Citanthauzo ca ‘Dzina lanu liyeretsedwe’ (10 min)

- Funsani aphunzi citanthauzo ca ‘Dzina lanu’ ndi ‘liyeretsedwe’.
- Fotokozani:
Dzina lanu = Dzina la Mulungu = Mulungu yekha
Liyeretsedwe = lilemekezedwe, likwezedwe
‘Dzina lanu liyeretsedwe’ citanthauza kuti tipemphera kuti dzina la Mulungu (ndilo Mulungu yekha) lilemekezedwe.
- Funsani anyamata ndi atsikana njira m’mene tingayeretse dzina la Mulungu.
Yankho: Tingalemekeze Mulungu m’zimene timacita ndi kunena.
- Fotokozani kuti m’phunziro iri tidzaganizira za kulemekeza Mulungu ndi mau athu.

3. Kugwiritsa nchito mau athu kulemekeza Mulungu (10 min)

- Uzani anyamata ndi atsikana kupatsa zitsanzo za m’mene tingagwiritse nchito mau athu.
Yankho: mwacitsanzo: kulankhula, kulangiza, kucita thonjo, kupempha thandizo ndi kupemphera.
- Afunseni ndi cifukwa ciani Mulungu anatipatsa mau.
Yankho: Mulungu anatipatsa mau kuti tizimlemekeza ndi kumtamanda. Ndiye tiyenera kulankhula motero kuti tilemekeza ndi kutamanda Mulungu.

4. Citanthauzo ca liu ‘aleluya’ (10 min)

- Funsani anyamata ndi atsikana citanthauzo ca liu ‘aleluya’.
- Fotokozani kuti liu ‘aleluya’ licokera m’Cihebri ‘Halleluya’. Cihebri ndi cilankhulo m’mene Baibulo linalembedwa poyamba. Liu ‘halleluya’ m’Cihebri litanthauza ‘Lemekezani Ambuye’. M’Baibulo liu ‘halleluya’ limagwiritsidwa nchito poulula ciyamiko ca Mulungu ndiponso polemekeza pa m’mene aliri ndi pa zimene acita (Cibvumbulutso 19.1 ndi 6, Salimo 106.1 ndi 48 ndi Salimo 150.6).
- Tiloledwa kugwiritsa nchito liu ‘aleluya’ pamene tilemekeza Mulungu cabe ndipo sitiloledwa kuligwiritsa nchito kuletsa dzungo m’mpingo. Ngati tigwiritsa nchito dzina la Mulungu mosayenera, sityeretsa dzina lake koma tacimwa!

5. Colowapo (10 min)

- Uzani aphunzi colowapo ici:
Judith ndi Faides akhala pa mphasa kutsogolo kwa nyumba. Ali kutandala. ‘Kodi munamvako nkhani ija ya Sara?’, afunsa Judith. ‘Mwamuna wake anafa mwadzidzidzi. Anthu anati kuti anacita kumuthirira’. ‘Inde, ndinamvako’, anena Faides. ‘Ndiganiza kuti

Sara anamva nsanje, cifukwa ndinamva kuti mwanuna wake anagona ndi atsikana ena azisumbali’.

- Pangani magulu anai.
- Gulu lirilonse ayankhe mafunso awa omwe mulemba pa bolodi:

Mafunso

1. Ndi ciani cimene cinacitika m’nkhani?
2. Kodi tingaliche bwanji chimo limene anacita?
3. Kodi m’udzi mwanu cimacitika kuti anthu akamba motere?
4. Nanga inu muli ndi makhalidwe otere?
5. Kodi Faides anafunika kumyankha bwanji Judith m’njira yabwino?
6. Ndi cifukwa ciani makambidwe otere ndi oipa?

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi.

Mayankho abwino ali conco:

1. Ndi ciani cimene cinacitika m’nkhani?

Yankho: Bwerezani mwacidule zimene zinacitika.

2. Kodi tingaliche bwanji chimo limene anacita?

Yankho: Anacita thonjo. Anakamba zinthu zopanda umboni. Komanso ngati tiri ndi umboni, sitiloledwa kukamba coipa ca wina aliyense ngati kulibe cifukwa ca kukamba tero.

3. Kodi m’udzi mwanu cimacitika kuti anthu akamba motere?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

4. Nanga inu muli ndi makhalidwe otere?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

5. Kodi Faides anafunika kumyankha bwanji Judith m’njira yabwino?

Yankho: Mwacitsanzo: sitiganizire koma timpemphere ndi kumthandiza Sara.

6. Ndi cifukwa ciani makambidwe otere ndi oipa?

Yankho:

- Makambidwe otere oononga cikhalidwe ca bwino ca munthu kopanda kudziwa ngati maganizo anu ndi oona.
- Makambidwe otere angakhale njira ya kudzikweza: si ndine woipa monga anthu ena.
- Mulungu afuna kuti anthu azikondana.

6. Kuwerenga Baibulo (30 min)

- Aphunzi atsegule Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Yakobo 3.1-12.
- Pangani magulu ang’ono-ang’ono. Auzeni kukambirana mafunso awa omwe mulemba pa bolodi:

Mafunso

1. Kodi Yakobo ananena ciani za malilime athu?
2. Fotokozani ndime ya 10.
3. Kodi mumasewenzetsa malilime anu momwe Yakobo ananena m’ndime ya 10?

- Kambiranani mayankho pamodzi. Mayankho abwino ali conco:

1. Kodi Yakobo ananena ciani za malilime athu?

Yankho: Ananena kuti malilime athu ndi monga tsihiro la combo cacikulu kapena monga moto. Pogwiritsa nchito tigiho laling'ono timayendetsa combo conse cacikulu. Cimodzimodzi ndi moto: kamoto kakang'ono kangatenthe nkhuhi zambiri. Cimodzimodzi ndi malilime athu: malilime athu ndi ang'ono, koma ngati tiwagwiritsa nchito mosayenera, tingabvutike komanso tingabvutitsa anthu ena.

2. Fotokozani ndime ya 10.

Yankho: Mulungu afuna kuti tigwiritsa nchito malilime athu kunena zabwino cabe. Safuna kuti tiwagwiritsa kunenanso zoipa.

3. Kodi mumasewenzetsa malilime anu momwe Yakobo ananena m'ndime ya 10?

Yankho: Aliyense ayankha pa yekha.

- Werengerani aphunzi 1 Yohane 3.18.
- Funsani aphunzi **citanthauzo ca ndime iyi**.
Yankho labwino liri conco: Tinganene kuti ndife Akristu kapena kuti tikonda Mulungu, koma tiyenera kuonetsa kuti ndife tero ndi macitidwe athu.

7. Kuchula Pemphero la Ambuye (5 min)

- Kambani pamodzi Pemphero la Ambuye mpaka onse adziwa.
Atate wathu wa Kumwamba
Dzina lanu liyeretsedwe
Ufumu wanu udze
Kufuna kwanu kucitidwe monga Kumwamba comweco pansu pano
Mutipatse ife lero cakudya cathu calero
Ndipo mutikhulukire ife mangawa athu, monga ifenso takhulukira amangawa anthu
Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo
Cifukwa wanu uli ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero wa nthawi zonse.
Amen.

8. Kutsiriza (5 min)

- Bwerezaninsu mwacidule citanthauzo ca 'Dzina lanu liyeretsedwe'.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene aphunzira lero zokhudza miyoyo yao.
- Pempherani.

Phunziro 3 – Ufumu wanu udze

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Coko
- Bolodi

1. Kulandiridwa (5 min)

- Landirani onse ndipo pempherani.
- Bwerezani mwacidule zimene zinakambidwa m’phunziro 2.
- Fotokozani kuti lero tidzaganizirako Mulungu Mfumu ndi ufumu wake. M’miyoyo yathu ya pa dziko lapansi mfumu ndiye munthu wofunikira wopambana. Ali ndi mphamvu zambiri. Anthu okhala m’dziko lake ayenera kucita malangizo ake. M’Zambia tiri ndi mafumu ambiri amene alamulira mbali zazing’ono za dziko lathu. Tiri ndi pulezidenti amene alamulira dziko lonse.

2. Kuganizira za kukhala pulezidenti wa Zambia (5 min)

- Uzani aphunzi onse kuganizira zimene afuna ngati ndiwo pulezidenti wa Zambia:
 - Kodi mungafune anthu a ku Zambia kucita ciani?
 - Kodi umoyo wanu ungaoneke bwanji?
 - Kodi mungacitire ciani anthu a ku Zambia?

3. Sewero: Ndani amene alamulira umoyo wanga? (10 min)

- Fotokozani kuti poona miyoyo yathu tingadziwe kuti zofunikira zoposa za ife ndi zotani (zinthu zimene timacita).
- Funsani anyamata kapena atsikana awiri kulemba pa bolodi zonse zimene amacita pa tsiku. Osatenga nthawi yaitali!
- Kambiranani momwe cingaoneke bwanji m’miyoyo yathu ya masiku onse ngati Yesu ndiye Mfumu yathu.
Yankho: Mwacitsanzo kupita ku calichi, kuwerenga Baibulo, kupemphera, kupempha Mulungu thandizo lake, kumuimbira, kumumvera.

4. Kufutokoza za ‘Ufumu wa Mulungu’ (20 min)

- Ufumu ndi malo olamuliridwa ndi mfumu. Ndiye Ufumu wa Mulungu ndi wolamuliridwa ndi Mulungu yekha.
- Fotokozani kuti Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi ndipo alamulira zonse ndi anthu onse.
Koma Adamu ndi Hava anasankha kucimwa, ndiye anasankha kukhala olamuliridwa ndi Satana, mdani wa Mulungu. Kucokera pa nthawi iyo anthu onse ali m’ufumu wa Satana ndipo cifukwa cake ticimwa. Mulungu ndiye Mfumu wopambana koma anthu ena alamuliridwa ndi Satana.
- Ufumu wa Mulungu uli ndi mbali ziwiri:
 1. **Ufumu wayamba kale kudza** (Luka 17.20 ndi 21, Mateyu 4.17). Pamene Yesu anali pa dziko lapansi anakonzanso Ufumu wa Mulungu mwa kugon anagonjetsa Satana ndi uchimo. Aliyense wokhululukidwa ku macimo ake ali m’ubwenzi watsopano ndi Mulungu ndipo akhala m’Ufumu wa Mulungu: Mulungu ndiye Mfumu wake.

Okhulupirira oona alamuliridwa ndi Mulungu ndipo amlondola Mulungu. Yesu atiuza kulowa m'Ufumu wake tsopano (Mateyu 6.33).

2. **Ufumu wake udzabwera.** Ufumu wa Mulungu sali kukhazikitsidwa mokwanira. Ufumu wake waulemerero udzaoneka pamene Yesu adzabweranso ku dziko lapansi. Zonse zidzakonzedwanso mwatsopano. Macimo ndi anthu ocimwa adzacotsedwa ndipo Mulungu adzalamulira bwino kwambiri m'ulemerero.
- Ndiye Ufumu wa Mulungu uliko mwa anthu obadwa mwatsopano komanso uli kudza. Ndi monga dzuwa: dzuwa lisanatuluke, kuunika kwake kuoneka kale. Cimodzimodzi: Ufumu wa Mulungu usanakhaleko mokwanira pa dziko lapansi, Ufumu wake uoneka mwa iwo obadwa mwatsopano.
 - Fotokozani citanthauzo ca pemphero 'Ufumu wanu udze'. Tipempha Mulungu kuti:
 1. Akhale Mfumu wathu wamunthu, kuti alamulira miyoyo yathu. Tidzipereka kwa Iye. Tipemphanso kuti anthu ena akhale m'Ufumu wa Mulungu kuti Ufumu wake wa pa dziko lapansi ukule.
 2. Yesu abwerenso pa dziko lapansi mosacedwa kuti akhazikitsa Ufumu wake mokwanira.

5. Kuwerenga Baibulo (20 min)

- Auzeni aphunzi kutsegula Baibulo ao. Osakhala m'magulu ang'ono!
- Werengani pamodzi Mateyu 6.33 ndi Macitidwe a Atumwi 16.31. Yankhani pamodzi funso iri:

Kodi Mfumu uyu amayembekezera ciani kwa ife?

Yankho: Afuna kuti timfunafuna. Tiyenera kumfunafuna poyamba m'malo mwa kukhala otangwanika ndi zonse za pa dziko lapansi.

- Werengani pamodzi Yohane 3.16 ndi Yesaya 53.3. Yankhani pamodzi funso iri:

Kodi Mfumuyo anaticitira ciani?

Yankho: Anadza pa dziko lapansi kuti afe pa mtanda.

- Werengani pamodzi Yohane 3.3 ndi Macitidwe a Atumwi 38 ndi 39. Yankhani pamodzi funso iri:

Kodi munalowa kale Ufumu wa Mulungu?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

Fotokozani kuti sitiri m'Ufumu wa Mulungu komabe ngati tabadwa mwatsopano. Nthawi zina anthu aganiza kuti ndiwo obadwa mwatsopano cifukwa ca ubatizo wao, koma ubatizo supangitsa anthu kukhala obadwa mwatsopano (mwa ubatizo tiulula kuti ndife Akristu obadwa mwatsopano). Yesu yekha asintha anthu kukhala obadwa mwatsopano.

- Werengani pamodzi 1 Akorinto 6.10 ndi Mateyu 7.21. Yankhani funso iri:

Kodi tingadziwe bwanji ngati tilondola Mfumuyo?

Yankho: Zipatso za m'miyoyo yathu zitionetsa. Ngati tingopitiriza kucita macimo olembedwa m'1 Akorinto 6.10, sitilondola Yesu. Koma cabe ngati ticita cifuniro cake. Akristu angacimwe, koma sapitirira m'uchimo.

- Werengani pamodzi Mateyu 28.18-20. Yankhani pamodzi funso iri:

Kodi Mulungu angakhale bwanji ndi omtsatira ena kulingana ndi ndime izi?

Yankho: Uthenga wake uyenera kulalikidwa. Anthu ayenera kumva Uthenga Wabwino wa Yesu Kristu kuti amdziwe ndi kumlondola.

- Werengani pamodzi Luka 10.2. Yankhani pamodzi funso iri:

Kodi m'Ufumu wa Mulungu muli udindo wa kwa inu?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha. Kuli udindo wosiyana-siyana, monga kuthandiza osauka, kuimba kwaya, kupyanga calichi, kulalikira ndi zina zambiri zimene ziyenera kucitidwa m'Ufumu wa Mulungu.

6. Kuphunzira za kubweranso kwa Yesu (20 min)

Aphunzitsi ayenera kukonzekera mbali iyi kunyumba mogwiritsa nchito 1 Atesaloniki 4.16-17, Cibvumbulutso 20.12, 2 Akorinto 5.10, Mateyu 12.36 ndi Mateyu 25.31-46 Pa nthawi yophunzitsa, fotokozani cabe cifukwa ca nthawi.

- Fotokozani zimene zidzicitika pamene Yesu adzabweranso. Fotokozani kuti:
 - o Pamene Yesu adzatsika Kumwamba anthu onse adzamva mau a mkulu wa angelo ndi mpfuu. Lipenga la Mulungu lidzamvanso.
 - o Yesu adzabwera m'ulemerero pamodzi ndi angelo onse.
 - o Iwo amene anafa mwa Ambuye (anthu obadwa mwatsopano) adzayamba kuuka kwa akufa.
 - o Yesu adzakhala pa mpando wake woyera m'ulemerero wamkulu. Adzakhala ndi mabuku ake. Aliyense ayenera kuonetsedwa ku mpando woweruza wa Yesu, cifukwa ciweruzo cidzakhudza anthu onse. Zonse zidzabvumbulutsidwa.
 - o Yesu adzalekanitsa anthu, monga m'busa alekanitsa gulu la nkhosa ndi abuzi. Gulu limodzi la anthu okhulupirira oona adzalandiridwa m'moyo wosatha m'Ufumu wake. Gulu lina (Iosapulumutsidwa ndi Yesu) adzakhala pa dzanja lamanzere lake. Iwo adzatamidwa ku Gehena.
- Fotokozani kuti sitikwaniritsa kudziyeretsa ku cimo lililonse (liu, ganizo, kacitidwe), koma tiyenera kulangidwa ku Gehena cifukwa ca macimo athu (Aroma 3.23). Ticimwa cifukwa mitima yathu ndi yocimwa. Tifunika Yesu kutiyeretsa ku macimo athu. Ngati tidalira pa Yesu kutipulumutsa ndi kutibweretsa m'ubwenzi ndi Mulungu, Yesu atenga macimo athu onse ndipo atiyeretsa kuti tikhala okonzeka kulowa Ufumu wa Kumwamba. Cipulumutso ca Mulungu ndi kwaulere! (Aefeso 2.8)
- Fotokozani kuti zabwino zathu sizitipangitsa kukhala Kumwamba koma zocita zabwino zathu ndizo zizindikiro za kukhala obadwa mwatsopano. Njira yeniyeni yokhala obadwa mwatsopano ndi kulowa Kumwamba ndiyo mwa Yesu amene anafa kukhululukira macimo a anthu ake. Macimo athu ayenera kucotsedwa tisanafe.

7. Lapani asanabwere Yesu (5 min)

- Funsani aphunzi ngati afuna Yesu kubweranso msanga.
- Fotokozani kuti Yesu adzabweranso pamene Uthenga Wabwino walalikidwa kwa mitundu yonse ya pa dziko lapansi (Mateyu 24.14).
- Fotokozani kuti Yesu ali kuyembekeza kubwera cifukwa safuna aliyense kuonongeka, koma afuna aliyense kulapa, kukhala okhululukidwa ndi kupita Kumwamba (2 Petro 3.9).

8. Kutsiriza (5 min)

- Bwerezani mwacidule citanthauzo ca 'Ufumu wanu udze'.
- Pempherani.

Phunziro 4 – Kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco pansi pano

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Coko
- Bolodi

1. Kulandiridwa

- Landirani onse ndipo pempherani.
- Bwerezinso mwacidule zimene zinakambidwa m’phunziro 3.

2. Kufotokoza za kucita cifuniro ca Mulungu

- Funsani anyamata ndi atsikana citanthauzo ca ‘kufuna kwanu’.
Yankho: Cifuniro ca Mulungu.
- Fotokozani kuti ticita cifuniro ca Mulungu pamene timumvera.
- Funsani anyamata ndi atsikana kuti tingadziwe bwanji cifuniro ca Mulungu.
Yankho: Cifuniro ca Mulungu cipezeka m’Baibulo. Pamene tiwerenga Baibulo, tidziwa cifuniro ca Mulungu. Kudziwa Baibulo lathu ndi kofunikira!
- Pamene ticimwa sitimvera ndipo siticita cifuniro ca Mulungu. Fotokozani kuti tingacimwe m’njira ziwiri:
 1. Ticimwa pamene ticita, tiganiza kapena kunena zimene Mulungu aletsa. Mwachitsanzo kuganiza za kuba ndi chimo, thonjo ndi chimo, kuganiza coipa ca munthu wina ndi chimo, kucita dama kapena cigololo ndi chimo.
 2. Ticimwa pamene siticita, sitiganiza kapena kusanena zimene Mulungu atilamulira. Mwachitsanzo kusathandiza ndi chimo, kusalemekeza Mulungu ndi chimo, kusathandizana ndi chimo, kusacita kalikonse pamene munthu wina amnyoza Mulungu ndi chimo.
- Funsani aphunzi ndi cifukwa ciani tipemphera ‘Kufuna kwanu kucitidwe, *monga Kumwamba*’.
Yankho: Angelo a Kumwamba ndiwo okonzeka kucita cifuniro ca Mulungu nthawi zonse. Ndiye pamene tipemphera pemphero iri, tipempha kuti tikhale okonzeka kucita cifuniro ca Mulungu nthawi zonse ndiponso m’ciriconse.
- Funsani aphunzi ndi cifukwa ciani tipemphera kuti kufuna kwa Mulungu kucitidwe.
Yankho: Cifukwa timkhulupirira kuti adziwa zabwino zoposa. Tikhulupirira kuti lye ndi wanzeru ndi wabwino. Tifuna kukhala odzicepetsa.

3. Colowapo (10 min)

- Awerengereni colowapo ici kuti amvetsetse:
Manuel amapita ku sukulu. Salifuna sukulu. Ku sukulu saikako nzero ndipo aphunzitsi amcenjeza katatu. Pobwera kucokera ku sukulu akomana ndi mwamuna wogulitsa malalanje. Njinga ya mwamunayo yagwa pansi ndipo malalanje amwazikanaponse. Manuel ampatsa moni mwamunayo ndipo apitirizabe ulendo wake. Pamene afika ku nyumba, akumva njala. Mai wake ampempha iye, ‘Manuel, pita kukanditengera tomato’. Manuel akana ndi kunena kuti, ‘lai, ndine wolema ndipo ndikumva njala’. Usiku wafika. Atasamba Manuel agwa pa bedi ndipo agona mwamsangamsanga. Baibulo lake likhala losatsegula.

- Kambiranani pamodzi mafunso awa:
 1. **Chulani zinthu zisanu zabwino zimene Manuel sanacite.**
Yankho:
 1. Sanaikako nzeru ku sukulu
 2. Sanathandize mwamuna
 3. Sanathandize mai wake
 4. Sanawerenge Baibulo pogona
 5. Sanapemphere pogona
 2. **Kodi mungadzilinganizire m'nkhaniyi? Ndi cifukwa ciani mwayankha tero?**
Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
 3. **Kodi cifuniro ca Mulungu kulingana ndi cifuniro cathu nthawi zonse?**
Yankho: Iai, nthawi zina cifuniro ca Mulungu cingatsutse cifuniro cathu.

4. Kuwerenga Baibulo (15 min)

- Fotokozani kuti Mulungu akamba kuti cofunikira kwambiri ndico kuonetsa zipatso za uzimu (mwacitsanzo Agalatiya 5.22).
- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Mateyu 7.17-23.
- Pangani magulu ang'ono.
- Lembani mafunso awa pa bolodi ndipo uzani aphunzi kuwayankha:

Mafunso

1. Fotokozani tanthauzo la ndime izi.
2. Kodi tingaphunzire ciani pa ndime izi?
3. Kodi aliyense amene anena kuti ndiye Mkristu adzalowa Kumwamba?

- Itakomana 5 minutes kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
 1. **Fotokozani tanthauzo la ndime izi.**
Yankho: Poona zipatso za mtengo tidziwa mtengo ndi wa mtundu bwanji. Cimodzimidzi kwa ife. Zipatso zathu zionetsa ngati ndife Akristu oona kapena Akristu onyenga.
 2. **Kodi tingaphunzire ciani pa ndime izi?**
Yankho: Ngati tinena kuti ndife Akristu koma sitionetsa zipatso zabwino (siticita cifuniro ca Mulungu) ndife anthu onyenga.
 3. **Kodi aliyense amene anena kuti ndiye Mkristu adzalowa Kumwamba?**
Yankho: Iai, koma ocita cifuniro ca Mulungu cabe.
Kumbukitsani aphunzi za phunziro 2 m'mene anaphunzira kuti zocita zathu sizitipulumutsa. Fotokozani kuti mizyu ya miyoyo yathu ifunika kukhala mwa Kristu (kudalira pa cipulumutso cake) kuti tibale zipatso zabwino (Yohane 15.1-6). Ndiye kucita cifuniro ca Mulungu kutanthauza kukhala mwa Kristu!

5. Zipatso (5 min)

- Pentani mtengo waukulu pa bolodi. Fotokozani kuti mtengowo ndi citanzo ca miyoyo yathu.
- Funsani aphunzi kupatsa zitsanzo za zipatso zabwino. Lembani mayankho ao m'mtengo. Lembani pansu pa mtengo zipatso zabwino zimene sitimacita nthawi zambiri.

6. Kutsiriza (5 min)

- Bwerezaninso mwacidule citanthauzo ca 'Kufuna kwanu kucitidwe monga Kumwamba comweco panso pano'.
- Funsani aphunzi zimene aphunzira lero zokhudza miyoyo yao.
- Pempherani.

Phunziro 5 – Mutipatse ife lero cakudya cathu calero

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Coko
- Bolodi
- Pepala kapena mwala

1. Kulandiridwa (10 min)

- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezaninso mwacidule zimene zinakambidwa m’phunziro 4.
- Fotokozani kuti lero tidzaganizirapo mbali ina ya pemphero la Ambuye: Mutipatse ife lero cakudya cathu calero. M’Pemphero la Ambuye poyamba tilemekeza Mulungu, kenaka tidzipempherera.

2. Kodi cakudya cathu calero ndi ciani? (15 min)

- Funsani aphunzi ngati adya cakudya ca m’mawa/masana asanabwere ku phunziro. Afunseninso cakudya cina cimene ayembekeza kudya lero.
- Fotokozani kuti cakudya cathu calero ndi cakudya cimene citithandiza kukhala moyo wabwino: cimene citipatsa thanzi. Cakudya cabwino ndi colengedwa ndi Mulungu, cipezeka m’cilengedwe ndipo matupi athu acifunika kukula. Cakudya cina conse cingakhale cokoma koma siciri copatsa thanzi ndipo si cakudya cathu calero. Tiyenera kudziwa ngati cakudya cathu ndi cabwino kapena coipa.
- Lembani mau awa pa bolodi (kapena pentani zithunzi):

Masweetie	Matomato	Kaloti	Soft drinks	Nsima
Mkate	Mabanana	Jiggies	Nsawa	Super dip

- Uzani mphunzi m’modzi kulemba mzere mozungulira cakudya cathu calero ndiponso kupha cakudya cimene si cakudya cathu calero
- Kambiranani pamodzi mayankho.

3. Kuwerenga Baibulo (35 min)

- Fotokozani citanthauzo ca ‘Mutipatse ife lero cakudya cathu ca lero’.
 1. Tipempha Mulungu kutipatsa zonse zomwe matupi athu afunika.
 2. Tiulula kuti cakudya ndi mphatso ya Mulungu.
 3. Tiulula kuti timadalira pa Mulungu. Kopanda dalitso lake, cakudya sicitikomera.
- Werengani pamodzi Salimo 145.15-16 ndi Macitidwe a Atumwi 14.17. Funsani funso iri ndipo kambirani pamodzi:
 1. **Kodi ndi yani amene apereka cakudya? Nanga apereka kwa yani?**
Yankho: Mulungu amapatsa cakudya kwa anthu onse ndi nyama zonse.
- Werengani pamodzi Mateyu 6.25-34. Funsani mafunso awa ndipo kambirani pamodzi:
 2. **Kodi tingaphunzire ciani kucokera ku ndime izi zokhudza Mulungu?**
Yankho: Zokhudza Mulungu tingaphunzire kuti ndi Iye amene amapatsa cakudya.

3. Kodi tingaphunzire ciani zokhudza zimene tiyenera kucita? Nenani zinthu ziwiri kapena zoculuka.

Yankho: Zokhudza ife anthu, tingaphunzire kuti tiyenera kukhulupirira Mulungu ndi kusadera nkhawa.

- Werengani pamodzi Miyambo 24.30-34, Salimo 128.1 ndi 2 ndiponso 2 Atesalonika 3.10-12. Funsani funso iri ndipo kambirani pamodzi:

4. Kodi ndi zooni kuti sitienera kugwira nchito kulandira cakudya cifukwa Mulungu amangopereka zimene afuna?

Yankho: Ndi bodza. Tiyenera kugwira nchito molimba ndipo sitiloledwa kukhala aulesi.

- Werengani pamodzi Masalmo 127.1 ndi 2. Funsani mafunso awa ndipo kambirani pamodzi:

5. Kodi tidzalemeradi ngati timagwira nchito molimbika? Ndi yani amene amapangitsa zinthu zimayenda bwino?

Yankho: Tingagwire nchito molimbika, koma tifunika dalitso la Mulungu. Kopanda dalitso lake, nchito yathu iribe phindu.

- Werengani pamodzi Miyambo 30.8 ndi 9 ndiponso Salimo 37.16. Funsani funso iri ndipo kambirani pamodzi:

6. Kodi cabwino coposa ndi kukhala olemera kapena osauka? Ndi cifukwa ciani mwayankha tero?

Yankho: Palibe kusiyana. Tikakhala osauka tiyesedwa kuba, koma tikakhala olemera tiyesedwa kuiwala za Mulungu ndiponso kudalira pa ndalama zathu.

7. Ndi ciani cimene cimapangitsa ife kukhala osangalala moonadi?

Yankho: Cotisangalatsadi ndi dalitso la Mulungu (Miyambo 10.22): ndife odalitsika ngati Mulungu ali nafe, ngati tapulumutsidwa ndi lye mwa Yesu Kristu. Ici sicitanthauza kuti tidzakhala miyoyo yathu kopanda bvuto (kumbukirani Yobu kapena Paulo m'Baibulo). Koma ngati Mulungu ali nafe, tiri ndi mtendere m'mitima yathu m'zonse zimene zingacitike.

- Afunseni funso iri:

8. Cifukwa ciani pemphero limati, 'cakudya cathu' m'malo mwa 'cakudya canga'?

Yankho: Sitiloledwa kukhala odzikonda: anthu ena afunikanso cakudya.

- Afunseni funso iri:

9. Ndi cifukwa ciani tipemphera kulandira cakudya cathu calero osati ca mawanso?

Yankho: Mulungu afuna kuti tibwera kwa lye mwa kupemphera masiku onse. Pemphero iri litsimikiza kuti timadalira pa lye m'zonse masiku onse (Eksodo 16.11-24).

4. Kufotokoza zina za mfundo ya lero (10 min)

- Fotokozerani aphunzi mfundo izi zofunikira:

1. Mulungu apatsa zimene tisowa. lye ndi wokhulupirika. Kudera nkhawi ndi chimo.
2. Tiyenera kugwira nchito kukapeza njira yopeza cakudya. Mulungu akuda ulesi.
3. Zonse zimene ticita zifunika kudalitsidwa ndi Mulungu, cifukwa zonse zopanda Mulungu ndi zacabe.
4. Mulungu ndi Atate wathu (akumbukitseni za ciyambi ca Pemphero la Ambuye). Mulungu ndi Mlengi wathu. Afuna kukhala m'ubwenzi nafe mwa Yesu Mwana wake. Afuna kuti tilankhula naye masiku onse. M'pemphero iri Mulungu atiphunzitsa za kudalira pa lye

ndi cisamaliro cake. Adziwa zimene tisowa. Cofunikira coposa ndi ubwenzi, si cakudya cabe.

5. Sewero (10 min)

- Sankhani m' modzi kupita pabwalo. Muuzeni kuti mudzampatsa kamkate (gwiritsani nchito pepala kapena miyala). Mphunziyo ayenera kusewera monga apatsidwa kamkate. Ayenera kukuyamikani pamene apatsidwa kamkate, kenaka adye ndi kusewera monga akutha asanatsirize kamkate (ndiye ayenera kutaya kamkate).
- Atatsiriza kusewera funsani aphunzi ena onse kunena njira ziwiri m'mene mphunziyo alakwa.
Yankho: sapemphera asanayambe kudya ndipo ataya cakudya (akumbukitseni kuti cakudya ndico mphatso yocokera ya Mulungu)

6. Kufotokoza Yohane 6.48-50 (15 min)

- Funsani anyamata ndi atsikani kuti angamve bwanji ngati akhala kopanda nsima tsiku limodzi, sabata limodzi kapena mwezi umodzi.
- Awerengereni Yohane 6.48-50. Fotokozani kuti mau awa ananenedwa ndi Yesu.
- Afunseni ndi cifukwa ciani Yesu ananena kuti lye ndiye Mkate wamoyo.
Mwacitsanzo mayankho otere:
 1. Sitikhoza kukhala ndi moyo kopanda cakudya ca masiku onse. Cimodzimodzi sitikhoza kukhala ndi moyo wa uzimu kopanda Yesu.
 2. M'masiku onse tifunika cakudya kawirikawiri. Ngakhale tingadye zambiri, matupi athu afunikanso cakudya cina patapita nthawi. Tifunika Yesu nthawi zonse. Sitifunika wina aliyense koma Yesu. Yesu yekha ndi Njira ya cipulumutso.

7. Kutsiriza (5 min)

- Bwerezaninso mwacidule citanthauzo ca 'Mutipatse ife lero cakudya cathu calero'.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene aphunzira lero zokhudza miyoyo yao.
- Pempherani.

Phunziro 6 – Mutikhululukire ife mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa anthu

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Bolodi
- Coko

1. Kulandiridwa (10 min)

- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezaninso mwacidule phunziro 5.
- Fotokozani kuti lero tidzaganizirapo mbali ina ya Pemphero la Ambuye: ‘Mutikhululukire ife mangawa athu (macimo athu), monga ifenso takhululukira amangawa anthu’.
- Funsani anyamata ndi atsikana zitsanzo ziwiri za anthu a m’Baibulo amene anapempha Mulungu kukhululukira adani ao.
Yankho: Mwacitsanzo Yesu (Luka 23.34) ndi Stefano (Macitidwe a Atumwi 7.60).

2. Kufutokoza za cikhululukiro (15 min)

- Fotokozani kuti kulingana ndi Baibulo anthu onse ndi ocimwa (Aroma 3.23, Mlaliki 7.20). Kucimwa kutanthauza kucita zimene Mulungu safuna komanso kusacita zimene Mulungu afuna. Mulungu akuda uchimo kotero kuti sakhoza kukhala pafupi ndi wocimwa, ngakhale wocimwayo acimwa kamodzi cabe. Koma ife tonse ticimwa kawirikawiri m’maganizo, mau ndi makhalidwe athu.
- Fotokozani kuti Mulungu akuda macimo onse, osati macimo akulu cabe. Afunseni kupatsa zitsanzo 20 za macimo, mwacitsanzo: kudzikweza, thonjo, kusamvera atsogoleri athu, kucita mwano, kudzikonda, kunyogodola, kusapembedza Mulungu, kusakhulupirira, kumvera mizimu, kucimwitsa wina ndi mnzake ndi cinyengo. Uzani aphunzi kulapa ku macimo ao ndi kupempha Mulungu cikhululukiro.
- Fotokozani za cikhululukiro. Cikhululukiro citanthauza kusinthana: Yesu atenga macimo a munthu wocimwa ndipo munthuyo apatsidwa ciyero ca Yesu kotero kuti Mulungu aona Yesu m’ malo mwa wocimwa. Munthuyo asanafike Kumwamba akhoza kucimwa, koma macimo ake onse ali pa Yesu. Ici sicitanthauza kuti munthuyo salabadira za macimo, koma awakuda kwambiri. Ngati munthu akumva bwino pocimwa, iye sanalandire Yesu Kristu monga Ambuye wake ndithu.
- Cikhululukiro cingamasuliridwe m’njira zosiyana-siyana:
 1. Mika 7.19: Mulungu ataya macimo onse a okhulupirira Yesu m’nyanja yakuya. Ici citanthauza kuti macimo ao onse acotsedwadi.
 2. Salimo 103.12: Mulungu acotsa macimo a anthu obadwa mwatsopano kotero kuti macimo ao sangawabvutitsebe.
 3. Yesaya 38.17: Mulungu saona macimo athu pali ife, cifukwa macimo athu ali pa Yesu ngati tiri mwa Iye.
- Limbikitsani anyamata ndi atsikana kuganizirako macimo ao, kulapa, kuwaulula kwa Yesu ndi kupempha cikhululukiro modalira pa mphamvu, cisomo ndi cikondi cake.

3. Sewero ndi kufutokoza za cikhululukiro (20 min)

- Awerengereni ziganizo zimene zalembedwa muni. Ngati mphunzi abvomera, ayenera kukweza dzanja lake. Ngati sabvomera sayenera kukweza dzanja lake. Aloleni kufotokoza ndi cifukwa ciani ayankha tero.
 1. **Munthu wina anaba za inu. Anakupemphani cikhululukiro. Munamkhululukira. Tsiku lina anabanso za inu. Nthawi ino simuyenera kumkhululukira.**
Yankho: Mulungu afuna kuti mitima yathu ndiyo yofuna kukhululukira ndi kuyanjananso.
 2. **Sitiledwa kuuza polisi ngati munthu alakwa koma tiyenera kumkhululukira.**
Yankho: Lamulo la dziko lathu la Zambia litiuza kuti mlandu wina wake uyenera kuuzidwa kwa polisi (e.g. kugwirira munthu kapena kupha munthu). Mulungu atipatsa anthu otilamulira kutilamulira ndi kuonetsetsa kuti kuli cikhalidwe cabwino. Anthu ocita zoipa ayenera kutsutsidwa. Kuyanjananso ndi kotheka cabe ngati wolakwa akumva cisoni (Luka 17.3: kudzudzula – kulapa – kukhululukira). Tiyenera kulakalaka nthawi zonse kuyanjana ndi kukhululukirana. Kuuza apolisi ndi kuyanjana sikutsutsana.
 3. **Sitiyenera kukhululukira iwo amene sakumva cisoni pa zimene anaticitira. Tiyenera kukhululukira otipempha cabe.**
Yankho: Baibulo likamba kuti tiyenera kukonda adani athu. Ngati wolakwa sapempha cikhululukiro kapena samvetsa kuti walakwa, kuyanjananso ndi kobvuta koma tiyenera kukhala olakalaka ciyanjano.
 4. **Mwana amene acita coipa sayenera kulangidwa. Makolo ake ayenera kumkhululukira.**
Yankho: Mwana ayenera kulangidwa cifukwa cilango ndi njira yophunzitsa makhalidwe abwino. Atalangidwa mwana ayenera kupempha cikhululukiro ndipo makolo ndi ana ayenera kuyanjananso. Kulanga kungacitike m'njira ziwiri:
 1. Mwa kukalipa, kopanda kudziletsa ndi kukwapula molimba (njira yoipa).
 2. Mwa cikondi, njira ya kuphunzitsa, modziletsa (njira yabwino).
 5. **Pamene mkazi acita coipa, mwamuna wake ayenera kumkwapula m'malo mwa kukhululukira.**
Yankho: Mkazi ndi mkulu amene anaphunzira kale zabwino ndi zoipa. Kuli njira zina zophunzitsa. Ayenera kuyanjananso. Mulungu ndi Mulungu wacifundo ndipo amuna azikhalanso acifundo (Aefeso 5.25).
 6. **Tifunika Mzimu Woyera kuti tiphunzire kupempha kukhululukidwa kwa macimo athu. Kopanda Mzimu Woyera tiganiza kuti siticita zoipa zambiri.**
Yankho: Zoon (Aefeso 2.1-10, Yohane 3.6).
 7. **Nthawi zina tipempha Mulungu cikhululukiro, koma sitikumva cisoni ceni-ceni pa macimo athu.**
Yankho: Mulungu adziwa zimene ziri m'mitima yathu. Adziwa ngati tikumvadi cisoni. Adziwa kuti ndife oipa kwambiri. Tiloledwa kumpempha kutiphunzitsa (Yeremiya 31.18 ndi 33, Aefeso 2.10).
- Malizitsani kukambirana ndi kufotokoza za cikhululukiro. Fotokozani kuti:
 1. Mfundo ikulu ya cikhululukiro ndiyo ciyanjano ca wolakwa ndi munthu wobvutika naye. Cikhululukiro si 'kusangoganizirako'.
 2. Cikhululukiro si citanthauza kuti macimo sayenera kulangidwa. Mulungu amakhululukira macimo mwa Yesu amene anasenza cilango ca anthu ake (kotero kuti kulibe cilango pali wocimwa). M'masiku onse munthu wolakwa ayenera kutsutsidwa ndipo nthawi zina ayenera kulangidwa (Aroma 13.1 ndi 4). Komabe kuyeneranso kukhala ciyanjano pakati pa wolakwa ndi wamene anabvutika naye.

3. Ngati wolakwa samvera cisoni pa chimo lake kapena ngati wobvutika safuna kukhululukira, si cotheka kuyanjananso koma kuyenera kukhala cilakolako ca kuyanjananso. Tiyenera kukhululukirana nthawi zonse (Mateyu 18.21 ndi 22).
4. Tifunika Mzimu Woyera kutiphunzitsa kupempha cikhululukiro. Sitikwaniritsa kucita cabwino ciriconse kopanda Mulungu yemwe. Mulungu afunadi kutiphunzitsa, ndiye tiyenera kumpempha zonse zomwe tasowa.

4. Nkhani (15 min)

- Fotokozani nkhani yolembedwa munsu:

Abusa tsiku lina analankhula ndi msirikali. Msirikali anali Mkristu weni-weni. Mbusa anamfunsa iye, ‘Kodi unabwera motani kwa Kristu?’ Msilikari anamuza nkhani iyi. ‘Msirikali mnzanga monga ine, anali munthu woopa Mulungu. Koma ine sindinali kumufuna iye. Ndinali kucita zinthu zambiri zoipa kwa iye kotero kuti anali m’nthawi zowawitsa.

Tsiku lina kunali mvula yaikulu. Msirikali mnzanga anabwera kucokera ku nchito yake usiku. Anali wolema ndi wobvumbidwa kwambiri koma iye asanagone anagwada pansu napemphera. Jombo zanga zinali zolemera ndi matope. Ndinatenga jombo yanga namumenya pa mutu. Kenaka ndinatenga jombo yanga ina namumenyanso pa mutu wake. Koma iye anapitirizabe kupemphera.

Tsiku lotsatapo ndinakhudzidwa popeza kuti jombo zosamalika bwino ndi kuzipolisha bwino zinali pafupi ndi bedi langa. Ndinazindikira kuti amene anacita tero ndi msirikali woopa Mulungu. Iyi inali yankho yake pa zoipa zimene ndidamcitira. Ici cinawawitsa mtima wanga woipa ndi wouma. Tsiku limenelo ndinalapa. Ndinacoka m’ucimo ndi mwa Satana napita kwa Mulungu. Ndinapempha Mulungu kukhululukira macimo anga onse’.

- Kambiranani pamodzi mafunso awa:

1. Yelekezerani kuti inu munali msirikali woopa Mulungu, msirikali amene anamenyedwa. Kodi munakacita ciani pa zocitikazo?
2. Kodi tingaphunziremo ciani m’nkhani imeneyi?
3. Kodi mudziwa zitsanzo za cikhululukiro m’umoyo wanu?

5. Kuwerenga Baibulo (40 min)

- Werangani pamodzi [Mateyu 5.38-45](#) ndi [Luka 17.3](#) ndi 4.
- Yankhani pamodzi mafunso awa:

1. **Kodi ndi kangati kamene tiyenera kukhululukirana?**

Yankho: Nthawi zonse. Miyoyo yathu iyenera kukhala wacikondi ndi wokhululukira.

2. **Fotokozani citanthauzo ca, ‘diso kulipa diso, ndi dzino kulipa dzino’?**

Yankho: Citanthauza kuti wolakwa ayenera kucitidwa cimene iye yemwe anacitira munthu wina. (Yesu anafotokoza kuti sitiloledwa kukhala obwezera cipongwe: sitiloledwa kupatsa cilango cacikulu pali colakwa cacing’ono, Mateyu 5.38-42).

3. **Fotokozani Mateyu 5.39.**

Yankho: Sitiloledwa kukhala obwezera cipongwe. Yesu afuna kuti tizikhululukirana ndi kukhala acifundo kuposa anthu osapembedza Mulungu. Tizikonda adani athu.

4. **Kodi ndi capafupi kucita zimenezi?**

Yankho: Nthawi zambiri kukonda adani athu ndi kobvuta. Ganizirani kuti Mulungu akonda adani ake (ndiwo ocimwa) ndipo yesani kucita cimodzimodzi mwa mphamvu yake.

5. **Kodi khalidwe lanu liri bwanji kuli adani anu?**

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

- Werengani pamodzi Aroma 12.14-21.
 - Yankhani pamodzi mafunso awa:
 6. **Kodi makhalidwe athu ayenera kukhala otani kuli adani athu?**
Yankho: tiyenera kuyankha mwa cikondi, modzicepetsa, mwa mtendere, mocita zabwino.
 7. **Werenganinso ndime ya 18. Kodi mumakhala ndi mtendere ndi anthu onse?**
Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
 8. **Fotokozani ndime ya 19.**
Yankho: Ngati tizindikira ndi kumvetsa kuti Mulungu aona zonse ndi kuti adzabvumbulutsa zonse pa tsiku la ciweruzo, tidzasiya zonse m'manja a Ambuye. Ngakhale zonse zosaoneka zidzabvumbulutsidwa.
 9. **Kodi tingagonjetse bwanji zoipa?**
Yankho: Mwa kucita zabwino kwa iwo oticitira zoipa (Aroma 12.21), monga m'nkhani ya msirikali woopa Mulungu.
 - Werengani pamodzi Mateyu 6.14-15.
 - Yankhani pamodzi funso iri:
 10. **Ndi ciani cimene cidzicitika ndi ife ngati sitikhulukira?**
Yankho: Ubwenzi wathu ndi Mulungu udzaonongeka. Ici sicitanthauza kuti kukhulukira wina kupangitsa Mulungu kukhala wotipatsa mitima yatsopano. Koma citanthauza kuti ngati Mulungu anatipatsa kale mitima yatsopano, kukhulukirana ndi kofunikira kwambiri kuti ubwenzi wa Mulungu ndi ife monga ana ake ukhalabe bwino.
- 6. Kutsiriza (5 min)**
- Fotokozani mwacidule citanthauzo ca 'Mutikhulukire ife mangawa athu monga ifenso takhulukira amangawa anthu'.
 - Afunseni zimene aphunzira lero zokhudza miyoyo yao.
 - Pempherani.

Phunziro 7 – Musatitengere kokatiyesa koma mutipulumutse kwa woipayo

Zofunikira pa nthawi yophunzira

- Baibulo
- Bolodi
- Coko
- (mayeso)

1. Kulandiridwa (10 min)

- Pempherani.
- Bwerezaninso mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m’phunziro 6.
- Funsani anyamata ndi atsikana citanthauzo ca ‘kuyesedwa’ m’pemphero iri.
Yankho: Kuputidwa kucita cinthu coipa.
- Afunseni kupatsa zitsanzo za mayeso.
Yankho: Mwachitsanzo kumwa mowa, kucita dama/cigololo, ufiti, kusamvera ndi kuba.

2. Kufotokoza za cikumbumtima (15 min)

- Fotokozani nkhanu iyi:
Tsiku lina Clement anayenda pa njira. Patsogolo pa iye panali munthu wokalamba nayenso ayenda. Dzina la wokalambayo ndi Aphiri. Aphiri anatenga cinthu cina kuturutsa m’thumba lake la thalauzi, koma iye sanazindikire kuti ataya K50 zimene zinagwa pa njira. Clement anayenda mofulumira kuthamangira ndalama. Anayang’ana uku ndi uku kudziwa ngati wina anamuona ndipo anaika ndalama izo m’thumba lace, la iye mwini.
Koma m’wana mwace Clement anapita kwa Aphiri ndi kubwezera ndalama zace. Clement ananena, ‘Dzulo inu munataya izi m’thumba lanu’. Aphiri anamfunsa, ‘Koma ndi cifukwa ndi ciani iwe sunasunge zimenezo? Sindinadziwe kuti ndidataya zimenezi. Kodi ndi ciani capanga iwe kukhala wokhulupirika ndi kubweretsa kwa ine?’
Clement anafotokoza, ‘M’kati mwanga ndinamva mau. Ndiri ndi munthu wabwino ndi munthu woipa mwa ine muno’. Clement anafotokoza, moloza cala cace pa cifuwa. Munthu wabwino mwa ine ndi cikumbumtima canga. Munthuyo wabwino anati, ‘Ndalama izi si zako, zibwezere’. Munthu woipa mwa ine anati, ‘Palibe bvuto kuti udatenga ndalama. Ndalama ndi zako’. Munthu wabwino anati: ‘Iai, iai, usasunge zimenezo’. Anthuwo anayambana m’kati mwanga. Sindinadziwe zocita. Kotero ndinapita kukagona. Koma munthu wabwino ndi munthu woipa anapitirizabe kulankhula ndi ine kotero kuti anandibvutitsa ine. Tsopano ndabweretsa ndalama, ndipo ndikumva bwino. Tsopano ndidziwa kuti munthu wabwino ndi wolongosoka.’
- Fotokozani kuti ‘munthuyo wabwino’ wochedwa ‘cikumbumtima’ amene asiyanitsa ndi kuonetsa zabwino ndi zoipa. Munthu aliyense ali ndi cikumbumtima. Kamau kang’ono komwe katiuza kusacita zoipa. Mulungu anatipatsa zikumbumtima. Zikumbumtima citithandiza kusiyanitsa zabwino ndi zoipa. Pamene tayesedwa tiyenera kumvera zikumbumtima zathu. Zikumbumtima zitithandiza kusankha zabwino.
- Fotokozani kuti ngati sitimvera zikumbumtima zathu, mitima yathu udzaumitsidwa. Kamau kang’ono kudzaleka kulankhula. Poyamba kamau ndi kwamphamvu koma ngati sitimvera, kamau kudzalankhula mosamveka ndipo kadzaleka. Ici cioneka mwachitsanzo pamene munthu wakupha samvera kuti walakwa. Ici ndi coopsya kwambiri.

3. Sewero (10 min)

- Pangani magulu awiri.
- Auzeni nkhani iyi ndipo uzani gulu limodzi kuyankha monga ndilo ‘kamau kwabwino’ ndi gulu lina monga ‘kamau koipa’.
Inu muli mu grade 9. Muyenera kulemba mayeso. Mayeso ndi yobvuta kwambiri ndipo inu simudwiza mayankho. Pafupi ndi inu pakhala anzanu amene ali ndi nzeru zambiri. Aphunzitsi sali ndi inu ndipo muli kuganizirako za kukopa mayankho a anzanu.
- Uzani magulu kukambirana, ndiye gulu lina liyenera kufotokoza kuti kukopa sikuloledwa (kamau kwabwino) ndipo gulu lina kuti kulibe bvuto kukopa mayankho (kamau koipa).
- Potsiriza afunseni zimene tiyenera kucita m’nkhani iyi.
Yankho: Sitaloledwa kukoperana, cifukwa ndi kuba (mayankho). Mulungu aona zonse.
- Auzeni nkhani ina ndipo uzani aphunzi kukambirana monga acita kale (kamau kwabwino ndi kamau koipa).
Muli pa nchito. Mwini sitolo akupemphani kuti mugulitse katundu. Iye akukhulupirira inu ndipo inu muli nokha m’sitolo. Lero mwagulitsa katundu ambiri ndipo muli nazo ndalama zambiri. Mau awiri ayamba kulankhula m’kati mwanu. Kodi anena ciani?
- Potsiriza afunseni zimene tiyenera kucita m’nkhani iyi.
Yankho: Sitaloledwa kuba. Mulungu aona zonse.

4. Kufotokoza za kupulumutsidwa kwa woipayo

- Afunseni citanthauzo ca ‘coipa’ ndi ‘woipayo’.
- Fotokozani kuti citanthauza: zonse zimenezi zitsutsa Mulungu: Satana, mitima yathu ndi zonse za pa dziko lapansi zimene siziri zoyenera pa maso pa Mulungu. Zonse zimene Mulungu akuda. Kulingana ndi cilankhulo coyamba ca Baibulo, pemphero iri litiuza kupempha Mulungu kuti atipulumutse kwa Satana.

5. Kuwerenga Baibulo (30 min)

- Aphunzi atsegule Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Marko 7.20-23.
- Yankhani pamodzi funso iri:
 1. **Zoipa zimacokera kwa Satana. Koma zimacokeranso ku cina cake. Kodi zimacokeranso kuti kulingana ndi ndime izi?**
Yankho: Zoipa zimacokeranso m’mitima yathu yocimwa. Yesu anati kuti zoipa zambiri zicuruka m’mitima yathu yocimwa. Kamau koipa m’kati mwathu si Satana cabe komanso mitima yathu yocimwa.
- Werengani pamodzi Tito 2.12.
- Yankhani pamodzi mafunso awa:
 2. **Zoipazo zimapezekanso pa dziko lapansi locimwa. Mulungu afuna kuti tizikhala osiyana ndi a dziko lapansi. M’Tito 2.12 tawerenga kuti tiyenera kukana cisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi. Perekani zitsanzo zina za zilakolako za dziko lapansi.**
Yankho: Zoipa zicokera kwa Satana, mitima yathu yocimwa ndi dziko lapansi locimwa. Zitsanzo za zilakolako za dziko lapansi ndizo: mowa, ndalama, dama/cigololo ndi zina zambiri.

3. Kodi Akristu ayenera kukhala osiyana ndi dziko lapansi m'njira yotani kapena m'zinthu zanzi?

Yankho: M'njira momwe amabvala zobvala ndiponso m'makhalidwe ao. Anthu ena aone kuti Akristu akhala pafupi ndi Mulungu.

- Werengani pamodzi Mateyu 26.41
- Yankhani pamodzi funso iri:

4. Funso: Cingatithandize ndi ciani kuti tithetse mayesero?

Yankho: Kucezera ndi kupemphera. Kucezera kutanthauza kukhala maso kotero kuti sitidzitengera m'mayeso, mwacitsanso kupita ku malo okumwako mowa kapena kukhala pafupi ndi abwenzi akuba.

- Werengani pamodzi Yohane 15.5.
- Yankhani pamodzi funso iri:

5. Funso: Kodi tingathetse mayesero m'mphamvu zathu pa ife tokha?

Yankho: Iai, sitikhoza kuthetsa mayesero pa ife tokha. Cifukwa cake timapempha Mulungu mphamvu yake. Tifunikadi thandizo la Ambuye Yesu Kristu amene ali wopambana koposa pakuti anafa pa mtanda nauka kwa akufa.

6. Kutsiriza (5 min)

- Bwerezaninso mwacidule citanthauzo ca 'Musatitengere kokatiyesa koma mutipulumutse kwa woipayo'.
- Ngati mufuna, aphunzi alembe mayeso.
- Tsirizani phunziro ndi pemphero.

Mayeso a Pemphero la Ambuye

Dzina.....

1. Ndi cifukwa ciani timapemphera?
 - A. Cifukwa tifuna cakudya
 - B. Cifukwa atsogoleri a mpingo afuna kuti timapemphera
 - C. Cifukwa tidalira pa Mulungu ndipo kupemphera ndiye njira yomlemekeza Mulungu
2. Pamene tikamba kuti, 'Atate wathu wa kumwamba' titanthauzanji?
 - A. Titanthauza kuti Mulungu ndiye Mlengi wa anthu onse ndiponso kuti anthu onse olapa ndiwo ana ake
 - B. Titanthauza kuti Mulungu ndiye Mfumu
 - C. Titanthauza kuti Kumwamba kuli Mulungu
3. Timapemphera 'Dzina lanu liyeretsedwe'. Pamene tipemphera pemphero iri tipemphera kuti
 - A. Onse adzamvera anthu olemekezeka ku chalichi monga atsogoleri a mpingo
 - B. Dzina la Mulungu lilemekezedwe
 - C. Makolo athu alemekedwe
4. Tingayeretse dzina la Ambuye mwa zimene timacita ndi
 - A. Kulankhula
 - B. Kuwerenga Baibulo
 - C. Kusaba
5. M'Yohane 3.3 tiwerenga, 'Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu'. Kodi kubadwa mwatsopano kutanthauzanji?
 - A. Kubatizidwa
 - B. Kulandira cikhululukiro ca macimo ndi mtima watsopano
 - C. Kuleka kuba
6. Pamene tipemphera 'Ufumu wanu udze', tipemphera pa zinthu ziwiri. Kodi timapemphera pa ciani pamene tipemphera 'Ufumu wanu udze'?
 - A. Timapemphera kuti Ufumu wa Mulungu wa pa dziko lapansi ukule ndiponso kuti Yesu adzabweranso msanga kukakhazikitsa ufumu wake
 - B. Timapemphera kuti mipingo idzakula bwino
 - C. Timapemphera kuti Mulungu adzalamulira bwino
7. Pamene Yesu adzabweranso tidzamva ndi kuona
 - A. Angelo ambiri kuimba nyimbo za Mulungu
 - B. Kulira kwa lipenga ndipo kuona Yesu Kristu pamodzi ndi angelo ambiri
 - C. Mzimu Woyera ngati moto
8. Anthu adzaweruzidwa. Kodi ndi anthu otani amene adzapita ku Mwamba?
 - A. Anthu amene anacitira anzao zinthu zabwino
 - B. Anthu amene anacita zinthu zabwino kuposa zinthu zoipa
 - C. Anthu amene analapa ndi kunalandira cikhululukiro ca macimo ao
9. Pamene timapemphera 'kufuna kwanu kucitidwe' timapemphera ciani?

- A. Cifuniro ca Mulungu cicitidwe
 - B. Kuti cifuniro ca matupi athu acididwe
 - C. Cifuniro ca makolo athu cicitidwe ndiponso kuti tikhale omvera makolo athu
10. Ndi ciani cimene ciri coona?
- A. Angelo a Kumwamba amacimwanso
 - B. Ticimwa pocita, polankhula ndi poganiza zinthu zoipa ndiponso posacita, posalankhula ndi posaganiza zimene Mulungu afuna
 - C. Kuganiza zoipa si cimo
11. Kodi tiyenera kucita ciani?
- A. Tienera kugwira ntchito kuti tidye
 - B. Tienera kukhulupirira kuti Mulungu atipatsa cakudya
 - C. Tienera kugwira ntchito ndi kukhulupirira Mulungu, kuti atipatse madalitso ndiponso kuti tilandire cakudya
12. Ndi cifukwa ciani timapemphera pa nthawi ya kudya?
- A. Cifukwa cakudya ndi mphatso yocokera kwa Mulungu ndipo tifunika dalitso lake pa cakudya kuti matupi athu adzadyetsedwe
 - B. Cifukwa abusa anena kuti tienera kupemphera
 - C. Cifukwa tifuna cakudya codalitsika
13. Kodi tiyenera kukhululukira adani athu kangati?
- A. 7
 - B. 7 x 70
 - C. Nthawi zonse
14. Ngati mwana acita coipa, sitienera kumpatsa cilango, koma kumkhululukira iye.
- A. Zoono
 - B. Bodza
15. 'Koma mutipulumutse ife kwa woipayo'. Kodi ndi zinthu zitatu zotani zimene zitanthauza kuti woipayo?
- A. Dziko locimwa, mitima yathu yocimwa ndi Satana
 - B. Satana, umfiti ndi zonse pa dziko zimene ziri zoipa
 - C. Mitima yathu, zonse pa dziko zimene ziri zoipa ndi anthu oledzera

Zikomo